## LANGUAGES AND LITERATURE DEPARTMENT

## MIYAMBI NDI MATANTHAUZO YAO

1. **Ulenje umasimba wako** = uyu mwambi woletsa kunama ngati wina aulula za anzake.
2. **Bvundula madzi** = munthu amene abweretsa udani pakati pa anthu.
3. **Khoswe akakhala pa mkate sapheka / mbalame ikakhala pa uta silasika** = Mlandu ukagwera banja la woweruza cimakhala cobvuta ukuuweruza.
4. **Galu wamkota sakandira pacabe** = Akulu-akulu ndiwo ali ndi nzeru zakuya.
5. **Umanena catsitsa dzaye poti njobvu ityoke mnyanga** = Mwambi wofuna kupeza yemwe wayamba kucimwa poti atenge ena kubwalo la mirandu.
6. **Kunena kwa ndithe-ndithe namnthambwe anazitengera** = Mwambi Wakuletsa kuyankhira nkhani za eni.
7. **Tsabola wakale sawawa** = Mwambi wonenedwa ndi anyamata ndi atsikana ponena kuti akulu alibe nzeru adakalamba.
8. **Mau akulu akoma atagera** =Mau aakulu amagwira nchito ngakhale Patapita nthawi .
9. **Patsala paja pagona cinziri** = Mwambi wotsutsa munthu amanena nkhani zakale zoithaitha.
10. **Nzeru nzayeka anabviika nsima m'madzi** = Munthu amafunika kufunsa kupambana kumangocita zinthu zimene satidziwa.
11. **Safunsa anadya phula** = Tiyenera kufunsa pa zinthu tisananene pena kucita cinthu cinthu cimene sitidziwa bwino.
12. **Kandimverere amanena za m'maluwa**=Mwambi wophunzitsa kusanena

Za mkamwa-kamwa koma zeni-zeni / Tiyenera kufunsa pa zinthu tisananene pena kucita cinthu cinthu cimene sitidziwa bwino.

13. **Cete-cete sautsa nyama** = Ndi mwambi woutsa nkhani pa mlandu.
14. **Nchenzi inamva mau oyamba** = Anthu pa mlandu amamva mau oyamba.
15. **Pawiri-pawiri sipauzirika** = Mwambi woletsa kusakaniza nkhani pa mlandu.
16. **Tsiku limodzi sililoza mbewa/ Lero lomwe linadetsa mnthengu** = Mwambi woletsa kuthamangira pakucita zinthu.
17**. Kulamula bvumbwe nkulinga uli ndi nkhuku** = Munthu poyamba mlandu afunika kukhala ndi poyembekezera.
18. **Tsoka msinde cimanga cilinda moto** = Mwambi wonenedwa ndi anthu amene ayesedwa mlandu koma sanalakwe.
19. **Ili kutali mvula mpesa umera m'ng'amba** = Cinthu ciri conse ciri ndi nthawi yake.
20**. Mubvi woyang'anira sucedwa kugwa m'maso** = Cinthu cobvuta ukaciyang'anira kufikira citakula mtsogolo usauka naco.
21. **Ndapakonda anasiya cikho mnnkhonde** = Mwambi wonenedwa ku munthu amene sanamvera malangizo coipa cisanafike.
22. **Mlendo ndi amene ayenda ndikalumo kakuthwa** = Nthawi zina mlendo akhoza kuthandiza atapatsidwa danga.
23. **Mbuto ya kalulu inakula ntadzaoneni** = Nkhani zina zimakula kamba kosinjirira.
24. **Kukana nsalu ya akulu nkubviika** = Kukanira munthu wamkulu momuzembezetsa kuti asacite manyazi.

25. **Mwana mnyanja alimbika mpani wake/Mpani wa mbewa utsatira mwini**.
=kawiri-kawiri poweruza milandu imakhala yoteteza acibale.

26. **Khoswe wapatsidwi anaulula wapadzala** = Mlandu umodzi ukhoza kuulula Ina yobisika.

27. **Mnthanga kunena anapisa likongwe wa a pongozi** = Mwambi wakuletsa kulonjereratu cinthu cobvuta kucitika kapena kukangaza kunena.

28. **Tinkanena anathira msiizi** = Mau woneneza munthu wotsutsa malangizo.

29. **Wakufa sadziwika** = Mwambi wakuletsa kunena mofulumira kapena modzitama.

30. **Kupulumukira mkamwa mwa mbuzi** = Mwambi wotsutsa munthu wonena bodza.

31**. Nyama yaliuma inafa ndi ludzu** = Mwambi wakuletsa kuumirira zinthu zimene zidzaononga moyo wako.

32. **Makale sapangana analira mthumba** = Cinthu ukapanda kucidziwa makhalidwe ake usaciyese cifukwa cingakutengere zobvuta.

33. **Nyalungwe cepsa kamnzake koma iye akapha ciwala acita cokoka** = Tisamacepetsa zinthu za anzathu ndi kukulitsa zathu.

34**. Nyumba yamwini saochera mbewa** = Zinthu zamwini ndizobvuta kuziyembekezera.

35. **Nguluwe idalira msampha utaning'a** = Mwambi wakuphunzitsa kupirira.

**36. Njobvu inagwa m'buna mwa aonenji/ Aonenji anapha njobvu ndi buma** /**Aonenji anapha mvuu m'mono** = Tisamasula kapena kucepetsa anzathu poganiza kuti sangaone kanthu kabwino popeza aliyense ali ndi mdalitso

wake.

**37. Waona nkhanga maanga wataya nkhwali =** Mwambi wakuphunzitsa Kukhutira ndi zomwe wapata.

38. **Cisoni cinapha msemamitondo /Cisoni cinapha nkhwali = Mwambi Wakuletsa** kucitira cisoni cinthu cimene ciri coopsa ndi cobvuta.

39. **Suzumire anaphetsa mkhala kale** = Tisamazolowezana ndi munthu wakhalidwe yoipa cifukwa angatibweretsere mabvuto.

40. **Kuipa kuombola** = Kanthu kalikonse kali ndi kufunikira kwake kapena mwai.

41. **Linda madzi ndipo uziti ndadala** = Mwambi wakuletsa kudzitama zobvuta zisanadze.

42. **Ndaonera momwemo mwambi wa gulugufe** = Kukhala ndi mtima wokhutira ndi zazing'ono.

43. **Nkhuyu zodya mwana zipota mkulu** = Mwambi wocenjeza akulu kulangiza ana ao cifukwa akabweretsa zobvuta naonso abvutikiramo.

44 **Kumbire ananka nawo** = Munthu asamangokhulupirira mnzake yekha.

45. **Okoma ngati fungwe** = Mwambi wonenedwa ndi munthu wodandaula amene zabwino zikayenera kukhala zao koma zaperekedwa kwa wosaziyenera.

46**. Pansi pamtima** = Mwambi umanenedwa ku munthu amene aopa kapena kucita manyazi kuulula zinsinsi.

47.**Wampota bwanji ndili kuula** = Mwambi wonyoza munthu wamithulu, waumbombo kapena womana.

48. **Wopusa amaomba ng'oma ocenjera nabvina** = Tisamanyoza anzathu cifukwa cakuonekera mopusa cifukwa wotereyo tsiku lina angaticititse

manyazi.

49. **Tsoka sasimba koma mwai** = Munthu aliyense asayese dala cinthu coopsya cimene cidzamtengera kuimfa.

50. **Saika mkute/kuika mkute nkutola-tola msana** = Sikuli bwino kumanena mnzathu wanjala kuti adyetsa.

51**. Mapanga awiri abvumbwitsa** = Tikapeza zinthu ziwiri koma tifunapo cimodzi, tiyenera kusankha bwino capamtima.

52. **Mamvera-mvera anacotsa Zolo pa ukwati** = Munthu asamangomvera ziri zonse anthu anena cifukwa adzataya zabwino.

53**. Wakwatira mende waleka citute** = Munthu pokwatira asamangoona nkhope yokha koma zazikulu monga moyo, nchito ndi mkhalidwe.

54. **Mako ndi mako usamuone kucepa mwendo** = Akulu ndi akulu tifunika kuwapatsa ulemu.

55. **Dombolo nkuombolana/ Mnthengu anaombola Namfuko** = Pamene mnzathu ali m'mabvuto pafunika kumthandiza.

56. **Konza kapansi kuti kamwamba katsike** = Munthu wofuna kukhala ndi zabwino ayenera kukonza zimene ali nazo.

57.**Muyang'ana dzuwa amasocera** = Munthu amafunika kufunsa pa zomwe sadziwa.

58. **Cala siciloza mwini** = Tikalakwa tiyenera kubvomera zolakwa zathu.

59. **Coka m'buyo khwangwala atole mphutsi** = Tisamacita mantha ndi zinthu zimene zingatibweretsere zabwino.

60. **Conona cimacokera kudzira** = Khalidwe la mwana limacokera ku makolo

ake.

61.**Ukapanda mano usamaswa mphale** = Cinthu ngati tiribe naco nchito tisamaononga cifukwa anzathu angathe kucigwiritsa nchito.

62.**Pamsasa saipitsa** = Sikwabwino kuipitsa pamalo ngati ticokapo cifukwa tikhoza kubwereranso.

63. **Pita uko sikuyenda** = Tikhala ndi anzathu, tizicitira pamodzi.

64. **Kupatsa ndiko kuika** = Munthu afunika  kupatsa anzake cifukwa tsiku lina iye akakasoweka zinthu anzakewo angamthandize.

65. **Masiku kuculuka, ubweya wanyama kucepa** = Munthu asamadzithama cifukwa sadziwa za mtsogolo.

66. **Mulereni aiwale kwao** = Tiyenera kusunga anthu bwino kuti asamakhala ndi maganizo ambiri.

67. **Tsoka liyambira  kumwendo** = Tsoka nthawi zina imayambira pa zinthu zazing’ono.

68. **Mafulufute akamatuluka, usatsinira kudzanje** = Ngati tifuna kupata zabwino ku anzathu sitifunika kuwacitira zoipa cifukwa angatibitse zabwinozo.

69. **Ukaipa dziwa nyimbo** = Ngati uli woipa pa zina, ufunika kukhala ndi pena pokomera.

70. **Anansi ndi nkhondo** = Nthawi zina anthu amalowa m’mabvuto kaamba ka anansi ake.

71. **Wakwata kwa mphenzi saopa kung'anima** / **walira mvula walira matope** = Munthu asamaopa zobvuta pa nchito popeza zabwino ziri zonse ziri ndi bvuto lake.

72. **Fisi anakana nsatsi** = Mwambi wumanenedwa ndi munthu amene akunamiziridwa ndi zimene sanacite.

73. **Msuma sudyera pomwe** = Mwambi wophunzitsa kusangako zinthu osatsiriziratu ndi kumbukira kumene unacokera.

74. **Nkhwangwa sithwera pa cipala** = Sicapafupi munthu kuti aoneke woposa anzake ngati ali mgulu koma akakhala panchito payekha.

75. **M'mimba ndi mcipala** = Zamkati palibe amene angazilamulire kuti koma zikanakhala zotere.

**76. Citsime cakale kuphera ludzu =** Sikwabwino kungokhulupirira zakale zokha.

77. **Ukoma ukadadza** = Tisamakometsera ndi tikakhazikika tasintha.

78. **Mtengo usamakoma pokwera pokha** = Tisamayambe cinthu tikalibe kuona matsiriziro ake.

79. **Pacedwa msulu pali nyerere** = Sikwabwino kucedwetsa cinthu polindirira wocedwa koma aziphunzira kuti cinthu ciri conse cirri ndi nthawi yake./Mwambi wophunzitsa cangu.

80. **Ici nciani nkulinga muli awiri** = Kuyenda awiri nkwabwino cifukwa wina akaona cozizwitsa akhoza kuuza mnzake.

81. **Cirimwe ndipatse munda** = Tisamathamangira zofewa zokha.

82. **Cibwenzi ca nkhwangwa cokoma pokwera pokha** = Tisamakonda munthu pamene tifunako zabwino kwa iye cabe.

83. **Udzu wobiriwira unapha mbuzi** = Munthu asapitirire muyeso wakukhuta.

84.**Thumba la tambe amasula ndi tambe yemwe** = Tisamaganiza kuti ndife

tokha anzeru, aliko ena anzeru monga ife.

85. **Kazitape** = Munthu wabodza.

86**. Sungani mwana** = Mau wocenjeza anthu kuti kwabwera mbala.

87. **Cala cimodzi siciswa nsabwe** = Tiyenera kuphunzira kuthandizana ndi anzathu.

88**. Malunje sadya sikwi** = Tisamacita ulesi cifukwa ca anthu ngakhale anzathu aticitsa ulesi.

89. **Njiwa usamasosolera pa msampha** = Tisamacita zinthu zimene zidzacenjeza anthu cifukwa ngati tatero angatithawe.

90**. Wachera ku mwezi/Osamagulitsana othyoka** = Tisamacitira zoipa anzathu cifukwa nawo angaticitire zoipazo.

91. **Mciuno mwa mwana simufa nkhuku** = Ulemu umapatsidwa ku munthu wamkulu osati wamng'ono.

92. **Tsamba likangwa manyazi agwira mtengo** = Mwambi wocenjeza munthu wocita zopanda zake, manyazkatenga zonse.

93. **Mwala wogumbundizika sumera ndere**. Munthu wosintha-sintha nchito malipiro ake sangakwere popeza umisiri wake sunakhazikike.

94.**Ukayendera nzengo usamati asakwi afumbula**= Tizitsatira zimene Tinayendera osati zina zake.

95. **Ndikhale nawo analandamalo**= Anthu ena pofuna kanthu amacita monyengerera pang'ono-pang'ono kufikira mtsogolo atenga zonse.

96. **Mfuno imodzi silowa zala** = Pafunika kucita cinthu cimodzi pa nthawi imodzi.

97. **Munthu ndi galu,galu ndi munthu** = kuyekeza munthu ali ndi zicito za agalu.

98.**Zafera m'mamadzira** = Uku ndiko kuti nkhani yangoponderezeka osaweruzidwa.

99. **Mlandu sagula ncipanda camowa** = Ucimo ndi ucimo osakondera poweruza mirandu.

100. **Ndikanadziwa kale ndikana phika therere** = Mau ocenjeza munthu kuti ayambe kucita zinthu zimene ali nazo m'malo mwakungokhala cabe.

101. **Mlendo ndi mame** = Tisamacitira alendo zinthu zoipa cifukwa iye ngosakhalitsa.

102.**Ukalemera usamanena m'cigulu** = Munthu aziphunzira kupatsa kuti ena angampatse mtsogolo.

103. **Ukasauka usamagwira nyanga** = Mwambi woticenjeza kuti tisamagwira nyanga pofuna kulemera.

104. **Konse-konse mpeni wansengwa** = Mwambi wonena zakugwirizana pa zinthu pa nchito.

ZIKOMO